Baibulo ya ana

Ikupasilani

Zozizwitsa za Yesu

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Byron Unger; Lazarus Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: E. Frischbutter; Sarah S.

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Yesu anachita zozizwitsa zambiri. Zozizwitsa zinali zizindikiro zosonyeza kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu. Chozizwitsa choyamba chinachitika paphwando laukwati. Panabuka vuto. Panalibe vinyo wokwanira aliyense.

Mariya, amake a Yesu, anamuuza za vutolo, kenako anauza antchitowo kuti achite chilichonse chimene Yesu analamula.



“Dzazani miphika iyi ndi madzi,” Yesu anatero. “Madzi?” mwina anafunsa. Inde, madzi ndi amene Yesu anapempha.

Kenako Yesu anauza wantchito wake kuti atenge mumphika umodzi waukulu n'kusiya woyang'anira phwando alawe. Madziwo tsopano anali vinyo! Vinyo wabwino! Vinyo wabwino kwambiri!

Atumiki adazizwa.
Yesu anasandutsa madzi kukhala vinyo. Mulungu yekha ndi amene akanatha kuchita zozizwitsa zoterozo.

Yesu anachita zozizwitsa zina. Tsiku lina madzulo, Iye ndi ophunzira ake anapita ku nyumba ya Petulo. Apongozi ake a Petro anali kudwala malungo.

Yesu anagwira dzanja la mayi wodwala uja. Kamphindi adachiranso. Ananyamuka kukatumikira Yesu ndi ophunzira ake.

Zikuoneka kuti mzinda wonse unasonkhana pakhomo madzulo amenewo. Anthu odwala anabwera - akhungu, ogontha, osayankhula, olumala. Ngakhale anthu amene anali ndi ziŵanda okhala mmenemo anasonkhana kwa Yesu. Kodi Iye angawathandize ochuluka chotero?

Yesu, Mwana wa Mulungu, akanatha kuthandiza. Yesu anathandizadi. Onse amene anabwera kwa Iye anachiritsidwa. Anthu amene ankangokhalira kuyenda ndi ndodo tsopano ankatha kuyenda, kuthamanga komanso kudumpha.

Ena anadza,
odetsedwa
ndi khate.

Iwo anakhala athanzi ndi oyera pamene Yesu anawachiritsa.

Amuna ndi akazi ogwidwa ndi ziwanda anaima pamaso pa Yesu. Analamula ziwandazo kuti zichoke kwa iwo. Pamene ziwanda zinamvera, anthu amantha, osasangalala anakhala bata ndi chimwemwe.



Kumbuyo kwa khamulo, amuna anayi anayesa kuthandiza bwenzi lawo kwa Yesu. Koma sanathe kuyandikira. Kodi akanatani?

Atanyamula munthu wodwala padenga la nyumbayo, mabwenzi okhulupirika anayiwo anang'amba tsindwi ndi kumutsitsa. Tsopano anali pafupi ndi Yesu.

Yesu anaona kuti anzake anayiwo anali ndi cikhulupililo. Iye alonga kuna munthu wakuduwala, "Madawo ako alekererwa. Nyamula mphasa yako, famba." Munthuyo anaimirira, ali bwino ndi wamphamvu. Yesu anali atamuchiritsa.

Pasanapite nthawi, Yesu anali m'ngalawa limodzi ndi ophunzira ake. Mphepo yamkuntho yoopsa inachititsa nyanja. Yesu anali mtulo. Ophunzirawo adagwidwa ndi mantha adamudzutsa Iye. Iwo anafuula kuti: "Ambuye, Tipulumutseni. Tiwonongeka!"

“Khalani chete,” Yesu analamula mafundewo. Nthawi yomweyo nyanja inachita bata. “Ndi munthu wotani uyu?” Ophunzira ake ananong'oneza. Ngakhale mphepo ndi nyanja zimamvera Iye. Anakhulupirira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu chifukwa zozizwitsa zake zinkasonyeza ulemerero wake. Ophunzirawo sankadziwa, koma



ankaona Yesu akuchita zozizwitsa zazikulu kwambiri pamene ankatumikira Mulungu pakati pa anthu.

Zozizwitsa za Yesu

Nthano yochokera mu mau a Mulungu,
Baibulo,

opezeka mu

Mateyu 8-9, Marko 1-2, Marko 4,
Luka 4, Luka 8, Yohane 2

“Polowela pa mau anu pamapasa kuwala.”
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16